**NYA_TTB_0806_script**

**Yesaya : 47:1-48:22**

**Mutu : Kugwa kwa Babulo ndi kubwerera kwa anthu wokhulupirira**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo m'dzina la Ambuye wathu Yesu Kristu. Tiyeni lero Ambuye atitsogolerere ndi mau ake apa Afilipi 3:12, pamene pali mau akuti, "Si kunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndathakukonzekawamphumphu; koma ndilondetsa, ngatinsondikachigwireichi chimeneanandigwirira Yesu Kristu."

Mupologalamu yatha tinali kukambirana pa Yesaya 45:1-46:9, za Kuyitanidwa kwa Koresi ndi chilango pa mafano onse. Ndipo lero pa Yesaya 47:1-48:22, tikambirana za kugwa kwa Babulo ndi kubwerera kwa anthu wokhulupirira.

**Yesaya 47**

Mu chapter 46, taona chilimbikitso chakuti a Yuda ayenera kuturutsidwa kuukapolo ku Babulo ndi kubwezeretsedwa ku dziko lawo.Pamene m'chapter 47, akufotokonzera za chilango chimene angapereke pa Babulo.Tere, chapter chonsechichadzala ndi

chithunzi cha momwe ufumu wodzikweza ungachititsidwiremanyazi.Tsono Babulo akuonetsedwa mwa chithunzi cha mkazi amene ndi wokongola ndi wokhala m'moyo wofewa.Ndiye pano Yesaya akuonetsa nyengo zomwe zimachititsa kuti munthu wodzikwezayuatsitsidwe.

1. Tsika, ukhale mfumbi, namwaliwe, mwana wamkazi wa Babulo; khala pansi popanda mpando wachifumu, mwana wamkazi wa Akasidi pakuti iwe sudzayesedwansowozizira ndi wololopoka.

Mau akuti "Tsika…" ndi mau amphamvu aulamulirowa Mulungu operekedwa kwa Babulo, monga muja amalamulidwiragalu. Umu, ndimomwe Mulungu adzalamulira Babulo pakugwa pake pamene nthawi ikwanira.Mulungu adzanena 'Tsika Babulo.'Tsono ndifuna mukumbukire kuti mau aulamuliro amenewa anaperekedwanso ndi Ambuye Yesu Kristu panthawi ya namondwepanyanja ya Galileya. Tamvani pa Marko 4:39, tipeza mau akuti, "Ndipo anauka, nadzudzula mphepo, nati kwanyanja, kuti; Tonthola, khalabata. Ndipo mphepo inaleka, ndipo kunagwabata lalikuru."

Tsono taonani kuti Babulo akutchedwa namwali chifukwa chakuti, anali asathiridwepo nkhondo ndikugonjetsedwa ayi. Kunena kuti Babulo akukula kumene kapena kutenga mphamvu, ngakhale ufumu wake ndiwakale, umene ukuchokera m'mbuyo ku Genesis 10, momwe umaonetsa Nimrod komanso mu Genesisi 11, m'meneukuonetsansanja ya Babulo. Tere pano Yesaya akuonetsa chithunzi cha kugwa koopsa kwa Babulo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani pano ikunena kuti Babulo wapalamulakwa Mulungu ndipo palibe wina amene angakhale naye paubwenzi. Babulo ayenera kudziwa kuti mau awa akunena ndi Mulungu, amene ali ndi kubwezera konse m'dzanja lake. Tere, ili ndi chenjezo lokwanira kuti ngati angalape, ndiye kuti akhoza kuletsa chionongeko chimenechi. Umu, ndimomwe ziri ndi inu ndi ine.Kunena kuti chilango chikudza ndithu pamunthu aliyense amene akangana ndi Mulungu.Komabe chisomo chochuluka chilipo kuti inu mukhoza kukonzanso ubale wanu ndi Mulungu, ndi cholinga chofuna kuletsa chilango kudza pa inu.

2. Tengamipero, nupereufa; chotsa chophimba chako bvulachopfunda, kwindam'mwendo, olokamitsinje.

Nkhani ilipanoikungoonetsa Babulo mwachithunzi cha namwali wolemekezeka, amene anali kutsitsidwa pansi, mwanjira ya usiwa ndi uchimo.Taonani pano namwali uyu, akuuzidwakugwira ntchito yopera, yomwe ndi ntchito ya akazi amene anali akapolo.Iyi, ndiyo nkhani ija inalembedwa pa Mateyu 24:41, imene ikuti, “Awiri adzakhala opera pamphero; m’modzi adzatengedwa, ndi wina adzasiyidwa.”Iyi, ndi ntchito yomwe inachokaku mayiko ya kum’mawa, yomwe amayigwira ndi akazi amene anali akapolo.Ichi, ndicho chithunzi cha momwe Babulo adzaonekera momwe adzaonongeke, ndi kutsitsidwa kufika pa mlingowakapolo.Izi zidzachitika chifukwa Babulo ndiye anazunza Israyeli ndipo nthawi yakwana kuti atsitsidwe.

Anzanga, ndifuna muonenso kuti Babulo adzatsitsidwa kufika poyendamaliseche.Ichi, ndicho chithunzi cha pomwe munthu wafika lero lino.Taonani munthu wafikapoyendamaliseche, koma osadzidzimuka konse.Tikunena munthu wamkulusakuchitamanyazi ngakhale akabvala ngati mwana.Ichi, ndichizindikiro chakutsitsidwa kuchoka pa munthu waulemerero kufika pakapolo.Pano ndifuna ndinenemotsindika ndithu kuti moyo

ndi mabvalidwe a munthu lero, akusonyeza kuchoka pa umunthu kufika pakapolo.Nkhani ikuti sizinachitikemwangozi kuti Mulungu amubveke munthu ayi, zinachitika chifukwa chofuna kuchotsa manyazi.Koma lero munthu akunena kuti, afunitsitsa kubwerera kumoyowamanyaziwo.Kodi inu mulibe ganizo limeneli?

3. Maliseche ako adzakhala osapfundidwa, inde, manyazi ako adzaoneka; ndidzachitakubwezera, osasamalira munthu.

Ndime iyi, ikuonetsa momwe mudzi wa Babulo udzaonekera pamene udzaonongeka. Kunena kuti kunyada ndi kudzikweza kwake konse kudzachotsedwa ndipo adzachititsidwamanyaziokha basi.Tsono izi, zidzachitika pa Babulo njira yopereka chilango chifukwa cha kudzikweza kwake ndi moyo wosoweka chikondi pa anthu a Mulungu, Israyeli.Pachifukwa chimene tikuona Mulungu akunenetsa kuti adzachita mosayang'ana nkhope, kapena kusamala za munthu wina ayi.Ndiye tikunena kuti Mulunguwaonetsa kutsimikiza mtima kuti aonongadi Babulo popanda munthu wina kumulepheretsa.Tsono kulimba mtima uku, ndikumenekukuonetsedwa pa Oweruza 8:21, pamene tipeza mau akuti, "Pamenepo Zeba ndi Tsalimuna anati, Tauka iwe mwini

nutigwere; pakuti monga munthu momwemo mphamvu yake.Ndipo GideonianaukanawaphaZeba ndi Tsalimuna, nalandamphande zinali kukhosi kwa ngamila zawo.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, tsono mwankhani yonseyi, tikuphunzira kuti iwo amene sagwiritsa bwino ntchito ulemu ndi mphamvu (udindo) yawo, ndiwo anthu ameneamaputa mkwiyo wa Mulungu kuti awatsitse.

6. Ndinakwiyira anthu anga, ndinaipitsacholowa changa ndi kuwapereka m’manja ako; koma iwe sunawaonetsera chifundo; wasenzetsaokalambagoli lako lolemera ndithu.
7. Ndipo unati, ndidzakhala mkazi wa mfumu wa nthawi zonse; ndipo sunasamalira izi mumtima mwako, kapena kukumbukira chomarizira chake.

Mundime izi, tikupeza Uthenga wakuti Mulungu akuonetsa poyera kuti Babulo anakhoza kapena kuti anachita bwino kutenga anthu a Mulungu chifukwa Mulunguyo analola kuti atero, osati chifukwa chakuti Babulo ndiwamphamvu ayi.Kutanthauza kuti Babulo anali kudzimva kuti anali ndi mphamvu zocholuka, kotero kuti anali kudzitama kuti anatenga Israyeli mwamphamvu yake.Apa,

ndipamene analakwitsa. Kunena kuti anali wosadziwa chimene Mulungu anali kuchita kudzera mwa iye.Nkhani ikunena kuti Mulungu anapereka Israyeli m'manja mwa Babulo chifukwa Israyeli anachimwa pamaso pa Mulungu. Mwanjira ina tikunena kuti chilango chimene Mulungu anapereka kwa ana ake, ndichimene chinanyenga Babulo kuti adzitamandire. Kunena kuti Babulo analikuganiza kuti anatenga Israyeli ukapolo mwamphamvu zake.Ndiye phunziro likunena kuti, anthu onse amene apatsidwa udindo kapena mphamvu, ayenera kuzigwiritsa ntchito moyenera chifukwa kanthu kamenekadauluka, kadzatsika kapena kadzatera. Ndiye tikutsindika kuti iwo amene ayenera kunyada, ayenera kunyada mwa Ambuye, amene sasintha konse.

8. Chifukwa chake tsono, imva ichi, iwe wotsatazokondweretsa, amene umakhala mosatekeseka, amene umati mumtima mwako, Ine ndine, ndipo popanda ine palibenso wina; sindidzakhala monga mkazi wamasiye, kapena kudziwa kumwalirakwa ana.

Pano ndifuna ndiyambe ndi mau akuti, Babulo anachita makani, nadzikweza ndi kuchita zinthu mosalabadira kuti chilango choopsa

kudza pa iye ayi. Ndikunena mau awa, chifukwa cha zomwe Nebukadnezara, mfumu ya Babulo ananena pamene anali kuona mudzi wa Babulo. Tamvani, iye anati, “Uwu, ndiwo mudzi waukulu ndi wokongola, umene ndaumanga ndi manja anga.” Kunena kuti sanapereka ulemu kwa Mulungu amene anamugwiritsa ntchito. Pachifukwa chimenechi, chilango chinamugwera Nebukadnezara, namuturutsam’mudzindikupitakutchire kumene anali kudya udzu ngati ng’ombe. Ichi, ndicho chilango chomwe Nebukadnezara analandira kuchokera kwa Mulungu chifukwa chodzitamandira.

10. Pakuti wakhulupirira zoipa zako, wati palibe wondiona ine; nzeru zako ndi chidziwitso chako zakusandutsa woipa; ndipo wanena mumtima mwako, ndine, ndipo popanda ine palibenso wina.

Pano ndiyambe ndi mau akuti palingozi nthawi zonse pamene mtundu wa anthu kapena munthu pa iye yekha adzazidwa ndi kudzikweza kuti akhoza kuchita chilichonse pa iye yekha. Taonani, wokondedwa kuti, lero tikukhala m’dziko momwe anthu akulemerakapena kupanga ndalamapakugwira ntchito yosayenera.Kunena kuti amagwira ntchito yowatsitsa, m’malo

mogwira ntchito yowalemekeza. Taonani pakati pathu palichisimo chakuti, bola kupeza ndalama. Pachifukwa chimenechi, anthu akuchita chiwerewere ngakhalenso kumagulitsamowa chifukwa chofuna ndalama.Komanso ena akuchita ntchito yogula ndi kugulitsa katundu koma mosalabadirachinyengo chomwe akugwiritsa ntchito.Izi, ndintchito zina zomwe ndizosayenera ngakhale timachitamobisa kapena kudziyeretsa, koma Mulungu akuona kotero kuti adzaweruza monga momwe anaweruzira Babulo.

12. Taima tsopano ndi maphendo ako, ndi unyinjiwamatsenga ako, m'menemo iwe unagwira ntchito chiyambireubwana wako; kuti kapena udzathakupindula, kuti kapena udzapambana.

Awa, ndi mau amene ndi wonyodola Babulo.Taonani Babulo ndiye wakhala akudalira ndi kugwiritsa ntchito matsenga ndi ufiti.Ndiye pano tsoka lamugwera, kotero kuti akuuzidwa kuti ayenera kuugwiritsa ntchito matsenga ndi ufiti wake kuti aletse chilangocho kuti apulumutsemudziwo. Mwanjira ina Mulungu akunena kuti Babulo anazamapakukhala ndi sukulu yophunzitsiramatsenga ndi

ufikipoganiza kuti ndiwofunika. Ndiye Mulungu akunena kuti tsopano nthawi yakwana ayenera kuyesa kuti aletse tsoka lomwe likudzali.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunena pano kuti iwo amene adzitamandira ndi kuchita zinthu mosalabadira Mulungu, ayenera kudziwa kuti tsiku likudza pomwe Ambuye adzanenakuti, gwiritsa ntchito nzeru yako kuti upulumuke. Awa, adzaoneka kuti ndi mau onyodola kapena olalata nthawi imeneyo.

13. Watopa mu uphungu wako wambiri; ayimirire tsopano opendazam'mwamba, oyang'ananyenyezi, akuneneratumwezi ndi mwezi ndi kukupulumutsa pa zinthu zimene zidzakugwera.

Pano mu Babulo mwagwachisokonezo monga mwatanthauzo la dzina la Babulo. Taonani mu Babulo mwachulukauphungu wosiyana-siyana, makamaka wochokera kwa anthu opendazam'mwamba, oyang'ananyenyezi ndi ena otere. Iwo anali kuchita izi ndi cholinga chofuna kuona mphamvu ya Mulungu kuti adziwezamtsogolo. Ndiye mwanzeru zimenezi Mulungu akuwauza kuti anthu amenewa ayenera kuteteza mudzi wa Babulo kuti adani

awo asaononge.  Mwanjira ina anthu amenewa sangathe kuchita chinthu china chokwanira kuletsa chionongeko cha Babulo.

Anzanga, nkhani iyi, ikukhudzanso inu ndi ine masiku ano. Taonani ifetikukhala m'dziko momwe tikudalirandalama kapena chuma basi, koma osaonacholakwa chathu.  Pano ndifuna kunena moona mtima kuti chisawawa chili m'dziko lathuli ndichifukwa chakuti ife ngati mtundu, tinachoka pamaso pa Mulungu woona. Koma taonani lero mudzi wa Babulo, umene sumatikhudzamkomwe, koma pano uli ndi Uthenga wochenjeza ife. Kunena kuti miyunda ya mudzi wa Babulo, ndiyo imene ikufuula kupereka chenjezo kwa inu ndi ine, kuti tiyenera kubwerera kwa Mlengi wathu.  Kutsimikiza kuti inu ndi ine, tiyenera kuphunzira kuchokera kucholakwa cha anthu ena.

**Yesaya 48**

Tsono magawo atatu otsirizawa ndiwo akutsimikizadi mau apa Yesaya 57:21, amene akuti, "Palibe mtendere, ati Mulungu wanga, kwa oipa."  Chimene ndifuna kunena ndichakuti Mesiya akudza ndi mtendere woposa chidziwitso chonse, ndipo anthu onse wokana Iye, sadzaona mtendere umenewu.Kunena kuti pamene munthu

ayambakupembedzamafano, ndiye kuti akuchoka pamanso pa Mulungu.Kutsindika kuti chipembedzo cha mafano ndicho chikutsogolera njira ya ku Babulo.

1. Imvani, inu banja la Yakobo, amene mutchedwa ndi dzina la Israyeli, amene munaturukam'madzi a Yuda amene mulumbira dzina la Yehova ndi kuchula dzina la Mulungu wa Israyeli, koma si m'zoona, penam'chilungamo.

Poyamba ndifuna kunena mau akuti, pali anthu ena, ameneamalimbikira kunena kuti Yuda ndi Israeli ndi anthu osiyana ayi, sizoona. Inu simuyenerakusintha dzina lomwe Mulungu anapereka.Taonani mundime tawerengayi, tikuona kuti Mulungu akulankhula ndi nyumba yonse ya Israyeli, yomwe inasankhidwa kudzera mwa Abraham, Isake ndi Yakobo.

Ndiye nkhani iyi, ikupita kwa a Yuda amene ali ku ukapolo ku Babulo, momwe akukumbutsidwa kuti iwonso ndiwochokera kwa kholo lawo Yakobo ndipo kuti ali ndi mwayi ofanana ndi Israyeli wa kumpoto.Taonani Yesaya akufanizira Yuda ndi mtsinje umene umatenga madzi ake kuchokera ku mtsinje waukulu.Ichi,

ndichifukwa chake akunena kuti, “amene munaturukam’madzi a Yuda.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, taonani dzina la Yuda likutchulidwa ndi cholinga chofuna kulemekeza komwe kumachokera mtundu wa Israyeli popeza ndiwo mtundu kumene kunachokera Mesiya. Tamvani mau apa Genesis 49:10, akunena kuti, “Ndodo yachifumu siidzachoka mwa Yuda, kapena wolamulira pakati pa mapazi ake, kufikira atadza Silo; ndipo anthu adzamvera iye.”

2. Pakuti adziyesaokha a mudzi wopatulika, ndi kudzikhazikitsaiwookha pa Mulungu wa Israyeli; dzina lake ndi Yehova wa makamu.

Tsono a Yuda amene anali ku Babulo, anali kudzitchula anthu wochokera ku mzinda woyera. Ndiye mwa mau amenewa tikunena kuti aliponso anthu wosalungama, koma amadzitchula wolungama chifukwa chakuti ndi membalawa mpingo. Koma ayenera kudziwa kuti sikukhalamembalawa mpingo kuti ndikumenekudzawapulumutsa ayi. Koma kukhala paubale ndi Kristu ndiko. Mau awa, ndi amene akutsindika kunena kuti

mitundu ina, imene ilibe chipembedzo chomwe chili ndi mphamvu yopulumutsa ndipo sadzapeza chipulumutso pamene aumilira ku mafano awo. Tsono chithandizo chawo chikupezekapakutembenukirakwa Mulungu woona basi. Ichi, ndicho chithandizo chawo komanso cha inu ndi ine.

Tsono nkhani iyi yafikaapa, chifukwa cha kupembedzakwachinyengo kumene a Yuda aonetsa. Ndiye Yesaya akunena kuti Mulungu afuna kuwaonetsa uchimo pazochita zawo pachipembedzo.Mlandu wonse akuwazengaukuchokera pakuti Yehova ndiye anawabala, ndipo ndiye amene wakhala akuwasamalira ndi kuwateteza, koma chifukwa ninji anthuwa akudza monyenga?Iwo, ayenera kudziwa kutiMulungu akudanandi mtima woonetsa ngati kuti akupembedza Mulungu woona, koma pamene mitima yawo ikupembedzamafano.Kodi mtima uwu, mulibe mwa inu?Koma muyenera kudziwa kuti chipembedzo chonyengachimunyasa Mulungu.

12. Mverani Ine, Yakobo ndi Israeli, oyitanidwa anga, Ine ndine; ndine woyamba, Inenso ndine womaliza.

Pano pali mau alonjezo kwa a Yuda omwe anali kuukapolo ku Babulo. Taonani Mulungu akulankhula kwa a Yuda onse kuti, ayenera kutcheramakutu kwa Iye, popeza ndiye Mulungu woona, amene analipo dziko lisanakhale ndipo adzakhalapokunthawiyamuyaya. Uyu, ndiye Mulungu amene akhozadi kukwaniritsa kuwaturutsa m'dziko la ukapolo.

22. Kulibe mtendere, ati Yehova, kwa oipa.

Mau awa, akuonetsa choonadi chonse chimene munthu wina sangathe kutsutsa.Tikunena kuti munthu akhoza kusangalala ndithu ndi kumatukuka ndithu m'chuma koma ndizinthu zimenezi zimachitika panthawi yochepa. Uwu, ndiwo ulemerero wa munthu wochimwa umene ukufotokonzedwanso pa Yesaya 57:20, pamene akunena kuti, "Koma oipa ali ofanana ndi Nyanja yowinduka; pakuti siingapume, ndi madzi akeautsamatope ndi ubve."

Wokondedwa anzanga apaulendo, titsirize ndi nkhani yakuti, madalitso atchulidwa mu verse 21, ndiwo ya ana a Mulungu.Kotero kuti palibe woipa ndi m'modzi yemwe angalandiremadalitsiwa. Kutsimikiza kuti kulibe mtendere kwa oipa onse. Kodi inu muufuna mtendere wa Kristu?

Lero tilekeza pano.  Ndipo timakambirana pa Yesaya 47:1-48:22, za kugwa kwa Babulo ndi kubwerera kwa anthu wokhulupirira.

Ambuye akupatseni inu mtendere wake.  Amen!